Examination No:______________________________

# LIKOLE EXAMINATION BOARD

**2022 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION**

## CHICHEWA

(100 Malikisi)

Thursday, 12th May

Nthawi: 2hr 15mins
01:00 – 03:15 pm

**Dzina Lanu:** ______________________________________________
(Dzina la bamboo koyamba)

**MALANGIZO**

1. Onesetsani kuti pepalali lili ndi masamba asananu ndi awiri**.**
2. Pepalali lili ndi magawo anayi; **A, B, C** ndi **D**.
3. Lembani kalata **kapena** chimangirizo mugawo **A** pampata omwe mwapatsiwa pansi pafunsolo. Ndipo muyankhe mafunso onse m'magawo **B, C** ndi **D.**
4. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C** m'mipata yomwe mwapatsidwa pansi pafunso lililonse.
5. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza limbo lokhonza pafunso lililonse.
6. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso (**Invigilator**) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 - 10 | | | |
| 11- 13 | | | |
| 14- 18 | | | |
| 19 - 23 | | | |
| 24 - 28 | | | |
| 29 - 32 | | | |
| 33 - 37 | | | |
| 38 - 42 | | | |
| 43 - 45 | | | |

**Examination No:**____________________________________

**GAWO A: MALIKISI 30**

**Langizo:** Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsimu. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere **100** komanso asadzole **150.**

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu: **'M'CHITIDWE OWONONGA KATUNDU PA SUKULU'**

Mwa zina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba.**
- Katundu yemwe ali pa sukulu panu
- Momwe sukulu yanu idamupezera katunduyo
- Omwe amawononga katunduyo.

**Ndime yachiwiri**
- Zomwe zimachititsa kuwononga katunduyo
- Kuyipa kwa mchitidwewu

**Ndime yachitatu**
- Momwe mungasamalire katundu pa sukulu panu.

**KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa a malume anu yowafotokozera za amayi awo omwe adadwala malungo masiku Apitawo.

Mwa zina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**
- Cholinga cha kalata
- Tsiku lomwe matendawo adayamba
- Momwe matendawo adayambira

**Ndime yachiwiri**
- Chithandizo chomwe odwalawo adalandila
- Zomwe mukufuna kuti amalumewo achite

**Ndime yachitatu**
- Malangizo omwe mudapereka kwa amayiwo pofuna kupewa matenda a malungo

________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________

Examination No:___________________________________

GAWO B (20 Malikisi)

**KUMVETSA NKHANI**

**3.** Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

Kalekale padali sukulu ina yotchuka kwambiri dzina lake Tikhozetonse. Pa sukuluyi padali Safuli ndi Kesho, atsikana a sitandade 8. Atsikanawa amakondana kwa chotsa phazi mpondepo. Ngakhale zidali chomwechi, atsikanawa adali ndi makhalidwe osiyana. Tsiku lina aphunzitsi awo a phunziro la Chichewa omwe adalembedwa kumathero kwa sabata, Safuli adapatsidwa mphatso yomwe idayikidwa m'chikwama cha saka pamene mnzake Kesho, mphatso yake idayikidwa m'chikwama chokongola kwambiri. Safuli sadasangalale ndi maonekedwe a chikwama chomwe mudali mphatso yake. Aphunzitsi atazindikira kuti Safuli sadasangalale ndi mphatso yakeyo, adamuuza Kesho kuti asinthane zikwamazo. Safuli adasangalala ndi maganizowo chifukwa chikwama cha Kesho chidali

chooneka bwino kwambiri. Atasinthana zikwama zija, aphunzitsi adawawuza kuti aliyense amasule kuti aone mphatso zomwe zidali mkati. Kesho atamasula chikwawa cha saka chija, adapezamo lamya yapamwamba kwambiri ndi ndalama zankhaninkhani . Safuli atatsekula chikwama chake chokongola chija adapezamo makope awiri ndi mapepala ojambulidwa zithunzi. Safuli adakwiya ndi kupsa mtima nafuna kulanda mphatso ya Kesho. Aphunzitsi ataona kuti Sufuli wapsa mtima adati, " Safuli, khala chete, tenga mphatso yomwe waipeza m'chikwama chako. Safuli, nthawi zonse uzikumbukira kuti chikomekome cha nkhuyu mkati muli nyerere"

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse

a. Kodi Safuli ndi Kesho ankaphunzira kuti?

_____________________________________________ 1 malikisi

b. N'chifukwa chiyani ophunzirawa adalandila mphatso?

_____________________________________________

_____________________________________________ 2 malikisi

c. Perekani chifukwa chimodzi chomwe Safuli adakwiyira ndi chikwama cha mphatso yake.

_____________________________________________

_____________________________________________ 2 malikisi

d. N'chifukwa chiyani aphunzitsi adawawuza atsikana aja kuti asinthane mphatso zawo

_____________________________________________

_____________________________________________ 2 malikisi

e. Perekani chifukwa chimodzi chosonyeza kuti Kesho adali mtsikana womvetsetsa.

_____________________________________________

_____________________________________________ 2 malikisi

f. Tchulani zinthu ziwiri zomwe zidapezeka m'zikwama muja

_____________________________________________ 2 malikisi

g. N'chifukwa chiyani Safuli adafuna kulanda chikwama cha mnzake

_____________________________________________

_____________________________________________ 2 malikisi

h. Pezani mawu m'nkhaniyi omwe akufanana m'matanthauzo ndi awa:

i) Msungwana _____________________________________1 malikisi

ii) Chola _________________________________________1 malikisi

i. Lembani khalidwe limodzi la Safuli

_____________________________________________ 1 malikisi

j. Perekani tanthauzo la chining'a ichi “chotsa phazi mpondepo”

_____________________________________________ 2 malikisi

k. Perekani phunziro limodzi lopezeka m'nkhaniyi.

_____________________________________________

_____________________________________________ 2 malikisi

## GAWO C: (10 malikisi)

**4.** Werengani malonje omwe ali m'munsiwa ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.

Nkhani yomwe tabwerera pano ndi yakuti akudandaula ndi makhalidwe oipa a ana athu, anawa sakumasamala katundu wa sukulu ndipo adaphwanyanso magalasi m'mazenera.

Tsopano yankhani mafunso awa:

a. Kodi ndi malonje anji mwawerengawa?
______________________________

b. Kodi malonjewa akuchitikira kuti?
______________________________

c. Kodi yemwe akuyankhura nkhaniyi ndi ndani?
______________________________

d. Kodi malonjewa akupita kwa yani
______________________________

e. Tchulani makaka awiri omwe amapezeka pa mbendera ya dziko la Malawi
______________________________

**5.** Pangano ziganizo zomveka bwino pogwilitsa ntchito mawu awa;

a. wanu
______________________________

b. fupa
______________________________

c. ndi
______________________________

d. msanga
______________________________

e. wapita
______________________________

## GAWO D (40 malikisi)

**Sankhani yankho loyenera pozunguliza yankho limodzi lokha A, B, C kapena D m'gawoli**

**Mafunso 6 mpaka 10:** Sankhani mitundu ya mawu amene atsekedwa mnzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**6.** A Zuze ndi a Singano ali ndi zigayo

**A.** Mneni **C.** Mlumikizi
**B.** Mperekezi **D.** Mvekero

**7.** Mwana wosamva amachititsa manyazi makolo.

**A.** Mfotokozi **C.** Mneni
**B.** Muonjezi **D.** Mlumikizi

**8.** Iye apita kwa achimwene ake mawa.

**A.** Mvekero **C.** Muonjezi
**B.** Mperekezi **D**. Mlumikizi

**9.** Hi! Mwana uja wagwa.

**A.** Mvekero **C.** Mfuwu
**B.** Muonjezi **D.** Mneni

**10.** Mtengo udagwa kuti khu.

**A**. Mneni **C.** Mvekero
**B.** Mfotokozi **D.** Mlumikizi

**Mafunso 11 mpaka 13**, Sankhani ntchito za mayina omwe atsekedwa nzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

**11.** Yohane akusewera mpira.
**A.** Mwininkhani **C.** Pamtherankhani
**B.** Mtsirizo wa mneni **D.** Wa malo

**12.** Fisi wagwira mbuzi
**A.** Loyitanira **C.** Mwininkhani
**B.** Mtsirizo wa mneni **D.** Pamtherankhani

**13.** Chimwemwe, bwera kuno.
**A.** Pamtherankhani **C**. Loyitanira
**B.** Mwininkhani **D.** Mtsirizo wa mneni

**Mafunso 14 mpaka 18**. Sankhani mawu oyenera kutsiriza mikuluwiko yotsatirayi

**14.** Za kumzinda _____________
**A**. Saulula **C**. Safunsa
**B.** Sakudya **D**. Sasankha

**15.** Kutola _______________ ndi m'mawa.
**A**. Mphalabungu **C**. Khobwe
**B.** Nkhuni **D**. Nyemba

**16.** Kuongola ____________ mpoyamba
**A.** Mtengo **C.** Bango
**B.** Miyendo **D.** Msana

**17.** Nkhuyu zodya _______ zidapota akulu.
**A.** Mnyamata **C.** Msungwana
**B**. Mwana **D.** Nkamwini

**18.** Chikumbutsa ___________ n'chisanu.
**A**. Jekete **C**. Nkhwangwa
**B.** Gombeza **D**. Moto

**Mafunso 19 mpaka 23** sankhani mtundu wa nthambi yomwe ili nzere kunsi mwake m'ziganizo zotsatirazi

**19.** Galu **amene akudwala** ndi wanga.
**A.** Yoyima payokha **C.** Ya mfotokozi
**B.** Ya dzina **D.** Ya muonjezi

**20.** Amayi adanena **kuti ndidziwerenga**
**A.** Ya mfotokozi **C.** Yoyima payokha
**B.** Ya dzina **D.** Ya muonjezi

**21.** **Nabanda akuwerenga buku** lomwe adagula.
**A.** Yoyima payokha **C.** Ya muonjezi
**B.** Ya dzina **D.** Ya mfotokozi

**22.** Sakudziwa **chimene akuvutikira ameneyu**
**A.** Ya dzina **C.** Ya muonjezi
**B.** Ya mfotokozi **D.** Ya mfotokozi

**23.** Adzabwera **pokhapokha mudzamuyitane**
**A.** Yoyima payokha **C.** Ya mfotokozi
**B.** Ya muonjezi **D.** Ya dzina

**Mafunso 24 mpaka 28**; perekani matanthauzo a zilapi/ndagi zomwe zili m'musizi

**24.** Nyumba yapsa mtanda wasala
**A**. Mwala **C**. imfa
**B.** njira **D**. makala

**25.** Ndimati ndichiponde koma chandiponda ine.
**A**. Madzi **C.** Mtengo
**B.** Matope **D**. Dothi

**26.** Sindidakawone m'mene kalowera m'mimbamu
**A.** Imfa **C.** Chakudya
**B.** Magazi **D**. Njala

**27.** Azungu atatu asenza galimoto
**A.** Mateyala **C.** Mafuwa
**B.** Mbaula **D**. Miyendo

**28.** Mbalame yayikira paminga
**A.** Lilime **C.** Tsoka
**B.** Chisa **D.** Njoka

**Mafunso 29 mpaka 32** Sankhani chiganizo chomwe chili ndi Zizindikiro zoyenera za mkalembedwe ziganizo zotsatirazi.

**29.**
**A**. Ogo! Madzi anga atayika.
**B.** Ogo! madzi anga atayika.
**C**. Ogo? Madzi anga atayika

**D**. Ogo Madzi anga atayika!

**30.**

**A.** Yohane amaweta, nkhuku , nkhunda, ndi mbira.

**B.** Yohane amaweta, nkhuku , nkhunda, ndi mbira.

**C.** Yohane amaweta, nkhuku , nkhunda ndi mbira.

**D.** Yohane amaweta nkhuku nkhunda ndi mbira.

**31.**

**A.** Kodi wadwala lero
**B.** Kodi wadwala lero?
**C.** Kodi wadwala lero.
**D.** Kodi wadwala lero!

**32.**

**A.** Maliya wapita kunsika?
**B**. Maliya wapita, kunsika.
**C.** Maliya wapita kunsika.
**D.** Maliya wapita kunsika!

**Mafunso 33 mpaka 37**; sankhani mitundu ya msintho wa aneni omwe ali ndi nzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**33.** Kapu yanga **idasweka**

| | |
|---|---|
| **A.** Womchitira | **C.** Wochititsa |
| **B.** Wochitirana | **D.** Wochitidwa |

**34.** Awa **amagonagona**

| | |
|---|---|
| **A.** Wochititsitsa | **C**. Wotsutsa |
| **B.** Wobwerezabwereza | **D.** Wochitidwa |

**35.** Namwali wa mwana uja **wamenywa**

| | |
|---|---|
| **A**. Wochititsitsa | **C**. Wochitidwa |
| **B**. Wonyazitsa | **D**. Wochititsa |

**36.** Mwana **wamasula** chingwe chija

| | |
|---|---|
| **A**. Wochititsitsa | **C**. Wochitirana |
| **B**. Wochitidwa | **D.** Wotsutsa |

**37.** Njinga zija **zaombana.**

| | |
|---|---|
| **A.** Wochititsa | **C.** Wochitirana |
| **B.** Wochitidwa | **D.** Wochititsa |

**Mafunso 38 mpaka 42.** Sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.

**38.** **Dzungu** lija lawola.

| | |
|---|---|
| A. Chi-, Zi- | C. Mu-, A- |
| B. Mu-, Mi- | D. Li-, Ma- |

**39.** Amayi agula **chinangwa** chokoma.

| | |
|---|---|
| A. I-, Zi- | C. Chi-, Zi- |
| B. Ka-, Ti- | D. U-, Ma- |

**40.** **Mwambo** wa chikwati udali wotsangalatsa.

| | |
|---|---|
| A. Mu-, Mi- | C. Mu-, A- |
| B. U-, Ma- | D. I-, Zi- |

**41.** Iye wataya **timiyala** tija.

| | |
|---|---|
| A. Ku – Pa – Mu | C. Ka-, Ti- |
| B. Li-, Ma- | D. Chi-, Zi- |

**42.** Nkhwangwa yagwera **m'madzi**.

| | |
|---|---|
| A. I-, Zi- | C. Chi-, Zi- |
| B. Mu-, A | D. Mu-, Mi- |

**Mafunso 43 mpaka 45.** Sankhani mitundu ya afotokozi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo.

**43.** Mnyamata **wamphamvu** akukankha galimoto.

| | |
|---|---|
| A. Wamaonekedwe | C. Waumwini |
| B. Wamakhalidwe | D. Woloza |

**44.** Njoka **ija** yaphewa ndi mphaka.

| | |
|---|---|
| A. Waumwini | C. Woloza |
| B. Wamakhalidwe | D. Wochuluka |

**45.** Aphunzitsi alowa m'kalasi **mwawo.**

| | |
|---|---|
| A. Woloza | C. Wamaonekedwe |
| B. Waumwini | D. Wochuluka |

**MAFUNSO ATHERA POMPA!!!**